



KAFUKUFUKU WA ANTHU A M'MIDZI YOKHUDZIDWA

----- Ndi -----

Mpatamanga Damu Projekiti



ZAMBIRI ZOKHUDZA MPATAMANGA DAMU PROJEKITI

Cholinga cha Mpatamanga Damu Projekiti ndi kumanga damu lopangira yamagetsi kuchokera ku mphamvu ya madzi pa mtsinje wa Shire. Gawo lina la projekitiyi ndi kumanga damu lachiwiri losungira madzi lomwe cholinga chake ndikuonetsetsa kuti makina opanga magetsiwo akulandira mulingo wamadzi okwanira. Padakali pano, ntchito yokonzekera kumanga madamu awiriwa ili mkati. Banki yothandiza popereka ndalama za chitukuko ya World Bank ili ndi chikonzero chofuna kuthandiza gawo lina la ntchitoyi popereka ndalama zokwana 350 miliyoni Dollars (pafupifupi 286 biliyoni Kwacha). Ndalama zonse zomwe zikufunikira kuti Projekitiyi itheke ndi 1.07 biliyoni Dollars (pafupifupi 874 biliyoni Kwacha).

Kuonjezera apo, boma la Malawi linapanga mgwirizano ongoyembekezera ndi banki ya IFC omwe unapangitsa kuti banki ya IFC ikhale ndikuthekera koyamba ntchito zina pomwe mbali ziwirizi zikuyembekezera mgwirizano okhazikika. Ma lipoti a IFC akuwonetsa kuti bankiyi inapereka ndalama ku projekitiyi. Gawo loyamba ndi la ndalama zokwana 3.5 million Dollars (pafupifupi 29 biliyoni Kwacha) pomwe gawo lachiwiri ndi la ndalama zokwana 4 million Dollars (pafupifupi 33 biliyoni Kwacha).

Projekiti ya Mpatamanga Damu ikhudza ndi kusokoneza moopsa kwambiri miyoyo ya anthu komanso chilengedwe cha midzi yozungulira. Zina zomwe zingakhudzidwe kwambiri ndi projekitiyi ndi izi:

- (i) Kusokoneza zachilengedwe za mu mtsinje wa Shire komanso kusokoneza umoyo wa anthu okhala mphepete mwa mtsinjewu omwe amawudalira mtsinjewu pa miyoyo yawo.
- (ii) Zinthu zina zomwe anthu amadalira kuti apeze chuma chothandiza umoyo wawo watsiku ndi tsiku zionongeka komanso malo okhala a mabanja ena akhudzidwa ndikusamutsidwa.
- (iii) Palinso chiyembekezere chakuti ntchitoyi ikhoza kuonjezera pa mavuto azachilengedwe omwe ntchito zina zikubweretsa monga zopanga mphamvu yamagetsi ochokera ku mphamvu ya madzi, ntchito zokhazikitsa ulimi wamthilira, ntchito zopopa ndikukonza madzi akumwa komanso kuononga nkhalango ndi zina zokhudzana ndi kusintha kwa nyengo m'malo ozungulira mtsinje wa Shire.

KODI KAFUKUFUKU WA ANTHU A M'MIDZI YOKHUDZIDWA NDI CHIYANI?

Kafukufuku wa anthu a m'midzi yokhudzidwa ndi ma projekiti ndi njira imodzi yomwe anthu okhudzidwa amagwiritsa ntchito kuti athane ndi mavuto omwe akukumana nawo kamba ka kubwera kwa ma projekiti amene akusokoneza miyoyo yawo. Pogwiritsa ntchito njirayi, anthu okhudzidwa amadalira nzeru ndi zinthu zomwe akudziwa zokhudza dela lawo pofuna kuzindikira vuto, kulilingalira vutolo komanso kuti apeze mayankho a vutolo ndikuwapereka kwa adindo. Ntchito ya mabungwe omwe si aboma pakafukufukuyu imakhala kuthandiza anthuwo kuyika mundondomeko zinthu zonse zomwe anthu amdelaro akuzipeza pomwe ntchito yeniyeni imakhala ya anthu okhudzidwa pokhala patsogolo kugawana nzeru pa zinthu zomwe akuzidziwa zokhudza delaro. Kachitidwe ka kafukufuku kotere kamagona mukuzindikira kuti midzi yokhudzidwa ili ndikuthekera kwakukulu kotsogolera ntchito yachitukuko chomwe akuchifuna mu midzi yawo.

KAFUKUFUKU WA ANTHU A M'MIDZI YOKHUDZIDWA NDI MPATAMANGA DAMU PROJEKITI

Mu Okutobala 2020, bungwe lomwe si laboma la CHRR mothandizana ndi bungwe lomwe si la boma lakunja la IAP linathandiza midzi yokhudzidwa ndi Mpatamanga Damu Projekiti kuchita kafukufuku owunika m'mene miyoyo yawo yakhudzidwira komanso ingakhudzidwire ndi projekitiyi. Anthuwa ndi ochokera m'midzi ya Chaswanthaka ndi Chikira m'boma la Blantyre komanso mudzi wa Kambalame mboma la Neno. Mu Malitchi 2021, bungwe la CHRR linachititsa misonkhano m'midzi itatuyi ndi kukambirana zotsatira za kafukufukuyu komanso kumva momwe ntchito zina zokhudza Mpatamanga Damu Projekiti zikuyendera.



Zimene zili mu lipoti ili ndi zokhazo zomwe anthu ochokera m'midzi yokhudzidwa anakamba.

ZOTSATIRA ZA KAFUKUFUKUYU

Pamisonkhano yomwe inachitika munthawi yakafukufukuyu, anthu a m'midzi yokhudzidwa ndi Mpatamanga Damu Projekiti anati sakutsutsana ndi ganizo lomanga projekitiyi. Anthuwa anati iwo ndiokondwa kuti pali ganizo lopanga projekiti imene ingathandize kuonjezera mphamvu ya magetsi mdziko muno. Komabe anthuwo ali ndi madandaulo komanso nkhawa zomwe akufuna kuti adindo amve ndikuchitapo kanthu poonetsetsa kuti projekiti ya Mpatamanga damu sikuwaphwanyira ma ufulu awo a chibadwidwe koma kuti ithandize kukweza miyoyo yawo.

1. ANTHU A M'MIDZI YOKHUDZIDWA SANAFUNSIDWE MAGANIZO AWO PA MA PULANI A PROJEKITIYI KOMANSO NDI MOMWE PROJEKITIYI IDZAYENDERE.

Misonkhano yomwe inachitika ndi anthu a m'midzi yokhudzidwa inawonetsa kuti anthuwo sanafunsidwe maganizo awo pa momwe projekitiyi ayikonzela komanso sanafunsidwe maganizo awo pa ma pulani komanso ntchito zina za chitukuko.

"Tinamva za projekitiyi kudzera mu Kafukufuku owona m'mene miyoyo yathu komanso za chilengedwe zikhudzidwire, m'modzi mwaotenga nawo mbali pakafukufukuyu anatero. Ndipo wina anati, "ine ndinamva za ntchitoyi kudzera mu mphekesera za anthu ena a m'mudzi muno."

Padakali pano anthu a m'midzi yokhudzidwa ayamba kale kuona zovuta zina kutsatira kubwera kwa projekitiyi. Mwachitsanzo mlatho waukulu wa m'mudziwu utakonongeka ndi mvula yamkuntho m'chaka cha 2019, anthu anamva kuti ntchito yomanganso mlathowu inayimitsidwa ndi a ku boma omwe akupanga ma pulani a Mpatamanga damu, akuti chifukwa chakuti mlathowu uli mkati mwa malo omwe amangepo projekitiyi. Apa, anthuwo akuyembekezera omwe akupanga projekitiyi kuti awauze momwe akuganizira zokonzala mlathowu kapena njira yomwe anthu a m'midziyi adziwolokera mtsinjewo. Anthu a m'midzi yokhudzidwayi akuti chifukwa chosowa mlathowu, pakali pano akugwiritsa ntchito mabwato akafuna kuwoloka mtsinje zomwe akuti zikuyika miyoyo yawo pachiswe ndipo ati anthu ena awiri amwalira kale atamila powoloka.

"Projekitiyi isanabwere, mvula inakokolera mlathowu ndipo a ku boma anabweretsa zipangizo pofuna kuwukonzanso koma omwe akupanga ma pulani a Mpatamanga damu anayimitsa ntchito yomanga mlathowu," anatero m'modzi mwa anthu a m'midzi yokhudzidwa.



2. ANTHU A M'MIDZI YOKHUDZIDWA SANAUZIDWE UTHENGA OFUNIKIRA OKHUDZA PROJEKITIYI KOMANSO MU NTHAWI YAKE

Malingana ndi zomwe kafukufukuyu wapeza, anthu 70 mwa anthu 100 aliwonse omwe anatenga nawo mbali pa kafukufukuyu anati alibe uthenga okwanira okhudza projekitiyi, ndipo 92 mwa anthu 100 aliwonse anati olo atafuna kudziwa zambiri za projekitiyi, sakudziwa kotu akatenge uthengawo.

“Boma silinapangitseko msonkhano wina uliwonse kuti atipatse ma uthenga oyenera okhudza projekitiyi.” M'modzi mwa anthuwo anatero.

Ngakhale kuti zambiri zokonzekera ntchitoyi zinayambika kalekale mchaka cha 2015, anthu okhudzidwa a m'midziyi akuti a nthambi yoona za magetsi ku boma sanapangitsepo msonkhano ofotokozera anthu a m'midziyi zambiri za projekitiyi. Anthuwa akuti akhala akulephera kutenga nawo gawo bwinobwino mu ntchito zosiyanasiyana zomwe zakhala zikuchitika pokonzekera projekitiyi chifukwa chosowa ma uthenga ofunikira oti awathandize kumvetisa zambiri za ntchito yomwe ikuchitikayi. Anthu anatinso omwe akugwira ntchitoyi amalimbikira kuwauza za ubwino okhaokha wa projekitiyi koma samawauza zovuta zomwe projekitiyi ingabweretse m'midzi mwawo komanso pa miyoyo yawo.

“Ndili ndi mafunso ambiri okhudza projekitiyi ndi momwe ikhudzile midzi yathu. Apa ndikupempha a ku boma kuti abwere kudzapangitsa misonkhano kuti tidzakambirane zambiri za nkhanayi kuti tiyendere limodzi,” anatero m'modzi mwa anthu amene anatenga nawo mbali pa kafukufukuyu, ndipo wina anati, “ine ndikufuna kudziwa zambiri za projekitiyi ndi mavuto omwe ingabweretse pa miyoyo yathu.”

Malingana ndi kafukufukuyu, 92 mwa anthu 100 omwe anatenga nawo gawo pakafukufukuyu anati sakudziwa amene akupereka ndalama zogwilira ntchito yomanga projekitiyi. 73 mwa anthu 100 aliwonse anatinso sakudziwa mwini wake wa projekitiyi pomwe 93 mwa anthu 100 aliwonse anati sakudziwa momwe angafikire mabungwe komanso a ku boma omwe akutenga nawo mbali pa projekitiyi. Iwo anati izi zikupangitsa kuti anthu a m'midzi yokhudzidwa asadziwe ma uthenga ofunikira a projekitiyi omwe akuwafuna monga:

- Ma ufulu a anthu a m'midzi yokhudzidwa komanso zomwe akuyenera kupindula kuchokera ku projekitiyi;
- Ma pulani a projekitiyi komanso ndi momwe projekitiyi idzamangidwire;
- malamulo okhudza momwe a ku boma akutengera malo a anthu kuti amangepo projekitiyi;
- Momwe ntchito yosamutsa anthu okhudzidwa itayendere, dongosolo la momwe adzalipilire anthu osamutsidwa komanso nthawi yomwe izi zichitike;
- Midzi komanso malo enieni omwe akhudzidwe ndi ntchitoyo;
- Mayina a mabungwe omwe agwire ntchitoyo, ntchito yomwe agwire ndi momwe anthu angawapezere;
- Momwe anthu okhudzidwa ndi ntchitoyi angapezere uthenga okhudza ntchitoyi komanso komwe angapeze uthengawu;
- Uthenga wa momwe ntchito yokumva maganizo a anthu ikuyenera kuyendera monga momwe malamulo adziko la Malawi okhudza ntchito zoterezi amafotokozera komanso mfundo za ma banki omwe akupereka thandizo la ndalama ku projekitiyi;
- Njira za ma banki ndi zina zomwe anthu angatsatire ngati ali ndi madandaulo okhudza ntchitoyi; komanso
- Zovuta zomwe zidzakhalepo m'midzi yozungulira chifukwa cha kubwera kwa Mpatamanga damu.

3. MIDZI YOKHUDZIDWA NDI NTCHITOYI SIIKUDZIWA NJIRA ZOTI ANTHUWO ANGAGWIRITSE POFUNA KUTULA MADANDAULO AWO.

Anthu okhudzidwa akuti ayamba kale kuona mavuto ena ndi ena okhudza ntchitoyi ngakhale kuti ntchitoyi idakali pa gawo longokonzekera. Ndipo mavutowa akuchitika chifukwa anthu sakudziwa zambiri zokhudza ntchito yomwe ikugwiridwa pa projekitiyi

Anthu a m'midzi ya Chaswanthaka ndi Kambalame akuti mu zaka zisanu zapitazi akhala akuona mavuto okhudza miyoyo wawo komanso kulemedwa m'maganizo chifukwa cha ntchito younika momwe projekitiyi idzakhudzire miyoyo komanso zachilengedwe yomwe inachitika poyamba. Kafukufukuyu anapeza kuti anthu 80 mwa anthu 100 aliwonse anafotokoza kuti ali ndi nkhwawa kwambiri kusiyana ndimomwe amamvera ntchitoyi isanayambe.



Anthu a m'midzi yokhudzidwa akuti anauzidwa kuti akakhala ndi madandaulo okhudza ntchitoyi akhoza kukadandaula kubwalo la milandu lilonse la m'dziko muno. Koma anthuwo akuti analetsedwanso kuchita izi ndi anthu omwe amayeza malo awo omwe anawauza kuti adzangotaya nthawi ndi ndalama kupita kubwalo la milandu ati chifukwa boma silingaluze. Izitu zikutsutsana ndi malamulo a dziko lino komanso ndi malamulo a ma banki omwe akuthandiza ntchitoyi ndi ndalama a IFC ndi World Bank pankhani yokhudza momwe anthu okhudzidwa angapezere thandizo pamavuto ena aliwonse okhudza ntchitoyi.

4. ANTHU OKHUDZIDWA SANAWAFOTOKOZERE MWANDONDOMEKO ZOKHUDZA KUSAMUTSIDWA KWAWO KOMANSO PALI ZOKHOTA ZAMBIRI ZOKHUDA NTCHITO YOKONZEKERA KUSAMUTSIDWA.

Anthu okhudzidwa akuti pali zokhota zambiri pankhani yokhudza kukonzekera kusamutsidwa kwawo monga;

- (i) kusauzidwa uthenga ogwirika pankhani yosamutsidwayi;
- (ii) kusabwera poyera ndikufotokoza bwinobwino momwe akuyezera malo a anthu okhudzidwa; komanso
- (iii) kusawafunsa maganizo awo pankhani yokhudza kusamutsidwa kwa manda omwe anakhudzidwa.

ZOMWE TIKUPEMPHA ADINDO KUTI ACHITE

Kafukufukuyu wapeza kuti anthu ogwira ntchitoyi sanalabadire zogwira ntchitoyi limodzi ndi anthu a m'midzi yokhudzidwa popanga dongosolo la momwe projekitiyi iyendere. Kuyendera limodzi ndi anthu a m'midzi yokhudzidwa kukutanthauza kuti anthuwa akuyenera kuwuzidwa ma uthenga onse ofunikira okhudza ntchitoyi ndi cholinga chakuti anthuwa adzitha kutenga nawo mbali popereka maganizo awo oyenera okhudzana ndi ntchitoyi komanso kupanga chiganizo choyenera chokhudza miyoyo yawo. Anthuwa akuyeneranso kuwuzidwa njira zomwe angatsatire kuti apereke madandaulo awo pa ntchitoyi.

Anthu okhudzidwa kukhala opanda ma uthenga okhudza projekitiyi ndi komwe kwabweretsa mavuto ambiri omwe anthuwa afotokoza mu kafukufukuyu. Kupeza ma uthenga ndi ufulu wa munthu wina aliyense. Gawo 19 la ndondomeko ya ufulu wa anthu ya bungwe lalikulu lowona ma ufulu wa anthu pa dziko lonse lapansi lotchedwa United Nations limanena kuti ndi ufulu wa aliyense *“kufunafuna, kulandira komanso kugawa uthenga ndi mfundo.”* Anthu a m'midzi yomwe yakhudzidwa ndi Mpatamanga Damu Projekiti ali ndi ufulu odziwa chili chonse chokhudza ntchitoyi ndi cholinga chakuti athe kupanga ziganizo zoyenera zokhudza miyoyo yawo komanso tsogolo lawo.

Tikupempha a ku boma la Malawi, ma banki a IFC ndi World Bank kuti ayike patsogo nkhanu yoti anthu adzitenga nawo gawo pa ntchitoyi poonetsetsa kuti akupereka ma uthenga oyenera okhudza ntchitoyi komanso munthawi yake. Monga momwe mfundo za bungwe la World Bank zokhudza kaperekedwe ka uthenga zimanenera, uthenga uliwonse okhudza ntchitoyi udziperekedwe muchilankhulo chomwe anthu okhudzidwawo amayankhula ndi kumva komanso mu ndondomeko zotsatira chikhalidwe cha dela lokhudzidwalo potengera zofuna zenizeni za anthu kapena magulu okhudzidwa mwanjira ili yonse, kuphatikizapo anthu olumala, osayankhula, a vuto lakumva ndi anthu osatha kuwerenga.

Zomwe Tikupempha Adindo A Ku Boma La Malawi Achite

- A ku nthambi ya za magetsi, chifukwa ndi omwe akukonza zokonzekera za projekitiyi, akhale pansi ndi anthu okhudzidwawa ndikuwafunsa maganizo awo pa ma pulani a Mpatamanga damu.
- Boma la Malawi likonze misonkhano yomva maganizo a midzi yokhudzidwa pa momwe adzapindulire ndi projekitiyi komanso m'mene angapitirizire kugwiritsa ntchito ndi kupindula ndi mtsinje wa Shire monga momwe amagwiritsira kale.
- A ku nthambi yoona za magetsi, chifukwa ndi omwe akukonza zokonzekera za projekitiyi, akonze misonkhano m'midzi yokhudzidwayo ndicholinga chofuna kufotokoza zonse zokhudza ntchitoyi.
- A ku nthambi yoona za magetsi akhale pansi ndi anthu am'midzi yokhudzidwa ndi ntchitoyi kuti akonze dongosolo la momwe anthuwa angaperekere madandaulo awo pa zovuta zomwe akukumana nazo ndi pa china chilichonse chokhudza ntchitoyi.
- A ku nthambi yoona za magetsi mogwirizana ndi anthu okhudzidwa ndi ntchitoyi akhazikitse dongosolo labwino lokhudza kasamutsidwe ka anthuwo, ndipo nkhwana zonse zomwe anthu afotokoza zokhudza ntchito yokonzekera kusamutsidwa kwawo ziunikidwe.
- Unduna owona zamalo ufotokozere anthu okhudzidwa ndi kusamuka za malamulo okhudza kusamutsidwa kwa anthu mogwirizana ndi ma ufulu ndi udindo wawo, dongosolo lakasamukidwe komanso mfundo zomwe zitsatidwe popeza malo omwe awasamutsire osayiwalanso ndondomeko za chipepeso chowasamutsira pa malo awo.
- A ku nthambi yoona za magetsi ayike mu ndondomeko zawo maphunziro a momwe anthu akuyenera kugwiritsira ntchito ndalama yachipepeso ndi momwe angasamalire ndalamayo kuti iwapindulire.
- Boma la Malawi likuyenera kuchita kafukufuku wa momwe projekitiyi ingakolezere nkhanza zomwe amayi ndi abambo amachitirana (kuphatikizapo pa nkhani yogonana ndi kugonana ndi atsikana achichepere) komanso kukhazikitsa dongosolo lolimbana ndi kuthetsa kwa nkhanza m'midzi yozungulira malo a ntchitoyi. Izi zikuyenera kuchitika ntchito yomanga malowa isanayambe.